**KUFOTOKOZA MWACHIDULE**
Kukonzedwa kwa Misonkhano ya Local Stakeholder Consultations ("LSCs") ya
**ZOCHITIKA ZA MA PROJEKITI A CARBON MWAUFULU ("VPAs") M'DZIKO LA MALAWI**
potsatira pulogalamu yomwe ikukonzedwa ya Gold Standard Programme of Activities ("PoA")
**"CLEAN COOKING BIOMASS SOLUTIONS PROGRAM FOR AFRICA"**

## Chiyambi

Kampani ya Burn Manufacturing Co, mabungwe ake ogwirizana ndi mabungwe ena okhudzana nayo ("Burn"), akukondwera kulengeza za misonkhano ya Local Stakeholder Consultation ("LSC") yokhudzana ndi ma VPA ake omwe akukonzedwa pansi pa Gold Standard m'Dziko la Malawi. Ma VPA amenewa adzakhala pansi pa GS PoA "Clean Cooking Biomass Solutions Program for Africa".

Dziko la Malawi limadalira kwambiri kugwiritsa ntchito biomass yomwe siibwerezedwanso (monga nkhuni ndi makala) pa kuphika m'nyumba. Kugwiritsa ntchito biomass m'nyumba kumakhala ndi zotsatira zoipa pa chilengedwe, kuphatikizapo kuwonongeka kwa nkhalango ndi nthaka, kuwonjezeka kwa utsi wa Greenhouse Gas ("GHG"), komanso kuchepa kwa chonde cha nthaka ndi kuthekera kwa nthaka kusunga madzi. Kuphatikiza apo, utsi wa m'nyumba (Indoor Air Pollution – "IAP") womwe umatuluka pamene nkhuni kapena makala zikuyaka ukhoza kuyambitsa matenda monga chibayo, sitiroko, matenda a mtima (ischemic heart disease), matenda a mapapo a nthawi yayitali (chronic obstructive pulmonary disease) komanso khansa ya mapapo.

## Cholinga ndi Ukadaulo wa Voluntary Project Activity (VPA)

BURN idzakhazikitsa ntchito za projekiti ya carbon ku Malawi pansi pa Gold Standard Programme of Activities (PoA) "Clean Cooking Biomass Solutions Program for Africa".

Cholinga cha VPA yomwe ili pansi pa PoA iyi ndi kufalitsa mbaula zamakono zogwira ntchito bwino kwambiri (Improved Cookstoves – "ICS") kwa makomo ku Malawi. Izi zidzaphatikizanso makomo omwe amagwiritsa ntchito mbaula zimenezi pa ntchito zing'onozing'ono zamabizinesi, monga malo odyera omwe amayendetsedwa m'nyumba.

Ma Greenhouse Gases (GHGs) ambiri, kuphatikizapo carbon dioxide, amapangidwa chifukwa cha kuyaka kosakwanira kwa biomass pamene imagwiritsidwa ntchito mu mbaula zachikhalidwe. Ukadaulo wa ICS womwe wapangidwa pa ma VPA uli ndi kuthekera kwabwino kopatsira kutentha kuposa mbaula zachikhalidwe zomwe zimagwiritsidwa ntchito poyambira. Izi zimathandiza kuchepetsa kuchuluka kwa biomass yomwe siibwerezedwanso yomwe makomo amagwiritsa ntchito kuti apeze mphamvu yofanana ndi yomwe imagwiritsidwa ntchito mu njira yakale.

Kuchepa kwa kugwiritsa ntchito biomass kumeneku kumathandiza kuchepetsa utsi wa GHG ndi IAP, komanso kumabweretsa phindu lina m'nyumba monga kuchepa kwa nthawi ndi ndalama zomwe zimagwiritsidwa ntchito kusonkhanitsa kapena kugula nkhuni kapena makala.

Pogwiritsa ntchito ICS, ogwiritsa ntchito amapereka ndikupereka ufulu wonse wokhudzana ndi carbon credits kwa BURN, yomwe yasankhidwa kukhala Coordinating and Managing Entity ya PoA komanso VPA Project Developer.

ICS zizagawidwa kapena kugulitsidwa mwachindunji kwa makomo omwe ali mkati mwa malire a projekiti.

**Gulu Lomwe Likuyang'aniridwa ndi Malo a Projekiti**

Gulu lomwe projekitiyi ikuyang'ana ndi makomo a m'mizinda, m'matauni kapena m'midzi omwe amagwiritsa ntchito biomass yomwe siibwerezedwanso mu mbaula zachikhalidwe (ndiye momwe zinthu ziliri poyambira) asanalandire ICS.

Malire a VPA akuphatikizapo madera a m'mizinda, m'matauni ndi m'midzi m'maboma onse 28 a Malawi.

**Ukadaulo**

VPA ikhoza kugwiritsa ntchito mitundu yosiyanasiyana ya ICS. Mbaula za ICS zimagwira ntchito bwino kwambiri, ndipo kapangidwe kake kamaganizira chikhalidwe cha anthu pa nkhani ya kuphika m'madera a projekiti, kuti kusintha kwa ukadaulo ndi kukweza moyo wa anthu zisawononge miyambo ndi chikhalidwe cha anthu.M'tsogolo, VPA ikhozanso kusankha kugawa mitundu ina ya mbaula pakapita nthawi.



ECOA MBAULA YA NKHUNI




ECOA MBAULA YA MAKALA

| UPANGIRI WA MBAULA | | |
|---|---|---|
| MLINGO | ECOA WOOD | ECOA CHARCOAL |
| Kusunga Moto | 53.7% | 71.3% |
| Cooking Power Output (kW) | 1.228kW | 0.956kW |
| Kuchepetsa tizitsotso zotulutsidwa pamene tikuphika | 210.2 mg/MJd | 38.16 mg/MJd |
| Kuchepetsa Utsi woipa wa Kaboni pamene tikuphika | 5.50 g/MJd | 3.78 g/MJd |

| | | |
|---|---|---|
| Chitetezo | 97.5% | 90% |

**Ndondomeko ya Kukhazikitsa**

- Kugawa mbaula za makono komanso za nkhuni kwayamba mu February 2025 ndi January 2025 motsatana. Kukayembekezedwa kuti pafupifupi 250,000 ICSs zidzagawidwa mpaka kumapeto kwa nthawi yoyamba ya crediting period.
- Local Stakeholder Consultations (LSC) zakonzedwa m'masiku atatu m'malo atatu osiyanasiyana ku Malawi motere:
    1. **Sogecoa Golden Peacock Hotel – Lilongwe pa 7 April 2026**
    2. **New Dawn Hotel – Lilongwe pa 8 April 2026**
    3. **Sogecoa Golden Peacock Hotel – Blantyre pa 10 April 2026**

Malo a Carbon Credits
Kuchepetsedwa kwa Greenhouse Gas (GHG) komwe kumachitika powonjezera kugwiritsa ntchito biomass zomwe sizingabwerezeke kudzabweretsa carbon credits motsatira malamulo ndi njira za certification.
Chuma chochokera kugulitsa carbon credits chithandiza pakati pa zinthu zina kuti:
a) Gawani mbaula zabwino pamtengo wotsika kuti ogwiritsa ntchito athe kuzilandira.
b) Kukulitsa ndikuwonjezera Pulogalamu, kufikira ogwiritsa ntchito ambiri.
c) Kupanga ntchito zambiri;
d) Kuyika ndalama mu R&D, kuti apange mbaula zapamwamba pamtengo wotsika;
e) Kupereka after-sales service yokhazikika komanso yodalirika.
f) Kuphunzitsa ndi kuonjezera chidwi cha ogwiritsa ntchito pa ubwino wa mbaula zabwino komanso momwe angazigwiritsire ntchito.

**Digital Monitoring, Reporting and Verification (DMRV)**

Kuti kuwonjezere kukhulupirika, zolondola, ndi kupezeka kwa malipoti pa carbon credit generation, VPA idzayambitsa Digital Monitoring, Reporting and Verification (DMRV) system pakulimbikitsa ntchito.
DMRV system imagwiritsa ntchito zida za digital data collection, geotagging, ma database otetezeka a cloud, ndi njira zolamulira kuti zitsatire kugawa mbaula, mfundo za ogwiritsa ntchito, komanso momwe mbaula zikugwiritsidwira ntchito (ngati zikugwira). Field enumerators amathandizira kukonza deta pogwiritsa ntchito zida zam'manja, kuchepetsa zolakwika zomwe zimachitika ndi mapepala, ndikuwonjezera data integrity.

DMRV framework imalimbikitsa kutsatira zofunikira za Gold Standard mwa:

- Kuwonjezera traceability ya mbaula zogawidwa
- Kukulitsa reliability ya kuchepetsedwa kwa utsi (emission reductions)
- Thandizo pa secure data storage ndi kukonzekera audit
- Kuwonjezera transparency kwa anthu okhudzidwa

Kuphatikiza kwa DMRV kumalimbikitsa efficiency ya monitoring ndikuthandizira kuperekedwa kwa carbon credits apamwamba komanso odalirika pansi pa PoA.

Kuthandizira Ku Chitukuko Chokhazikika Cha M’dera




Kupatula kuchepetsa utsi woipa woononga chilengedwe, polojeketiyi ikugwirizana ndi zolinga za bungwe la United Nations mu mfundo zachitukuko chokhazikika (Sustainable Development Goal) ya nambala khumi ndi zitatu (13) "*Kupanga changu pokhazikitsa mfundo zolimbana ndi kusintha kwa nyengo”*. Polojeketiyi ithandiza kutukula ma banja akumudzi komanso kusamala chilengwedwe nthawi yaitali.

Polojeketiyi ithandiza mfundo zachitukuko zokhazikika mu njira izi:

1. Kuchepetsa ndalama zomwe mabanja amagwiritsa ntchito pogula nkhuni kapena makala pophikira. Izi zikugwirizana ndi cholinga choyamba (1) cha mfundo zachitukuko “Kuthetseratu umphawi wamtundu wina uliwonse, kulikonse”.

2. Kuchepetsa Utsi woopsa wa kaboni monokisaidi pamene tikuphikira m’nyumba zomwe zizapangitsa kuti matenda achepe omwe amadza chifukwa cha utsiwu monga matenda ovutika popuma, Mutu komanso kuyabwa kwa maso pamene amayi ndi ana omwe amatenga gawo lalikulu pophika pakhomo. Izi ikugwirizana ndi cholinga chachitatu (3) cha mfundo zachitukuko chokhazikika

3. Kupititsa patsogolo umoyo wabwino wa anthu onse ndi cholinga cha chisanu (5) - Kukwaniritsa ndondomeko za kusasankhana pakati pa amayi ndi abambo ndikuwapatsa amayi ndi atsikana mwayi wodziyimira pawokha.

4. Kuchulukitsa kupezeka kwa luso la makono ndi lodalirika lophikira. Cholinga cha chisanu ndi ziwiri (7) - Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza mphamvu yodalirika, yokhazikika, yamakono ndi yotsika mtengo

5. Komaso kudziwitsa anthu za ubwino, chitetezo, chuma ndi kusamala chilengedwe zomwe zimabwera chifukwa cha kugwiritsa ntchito mbaula zimenzi. Cholinga cha chinayi (4) - Kulimbikitsa ndi kupititsa patsogolo mwayi wamaphunziro abwino kwa wina aliyense.

6. Mbaula zimathandiza anthu kupeza ntchito zosiyanasiyana m'maiko omwe kuli polojeketiyi. Cholinga choyamba (1) - Kuthetseratu umphawi wamtundu wina uliwonse, kulikonse komanso Cholinga cha chisanu ndi zitatu (8) - Kupititsa patsogolo chuma ndi kupezetsa ntchito zabwino zokhazikika kwa anthu onse.

7. Kuchepetsa kudula mitengo mwa chisawawa, kusamalira nkhalango zonse, kubwezeretsa nkhalango zowonongeka m'madera omwe amagwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku nkhuni kapena makala. Izi zithandiza kuti chilengedwe sisungike bwino komanso kuthandiza za chilengedwe zopezeka m'mapiri, kusungika kwa madzi komanso nthaka. Cholinga cha khumi ndi zisanu (15) - Kuteteza, kubwezeretsa, ndi kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito ka za moyo za pa mtunda ndi kusamala nkhalango, kuthetsa chipululu ndi kuwonongeka kwa nthaka)

**Kutsatira mfundo za ndondomeko ya Chitetezo**
Kuwunikira mokwanira mfundo za dongosolo ya chitetezo kuchitika pofuna kutsatira malamulo a chitetezo a Gold Standard, komanso kulemekeza malamulo, chikhalidwe, komanso malamulo onse a m'dera.

**Mfundo zikulu-zikulu zoyenera kutsatira zalembedwa munsimu mwa chidule motere;**

**Mfundo za Chikhalidwe cha Anthu**

- Mfundo yoyamba: Ufulu wa Chibadwidwe: Kugawa kwa mbaula za makono kapena zochitika zili zonse zili mu pulogalamu imeneyi kulibe kuthekera kwakuti kutha kuphwanya ufulu wa chibadwidwe, kapena malumbiro a maiko olimbikitsa ufulu wachibadwidwe. Zonse ziyenda monga imakambila mfundo za dongosolo la chitetezo a Gold Standard for Global Goals. Pa nthawi imene kuzakhale msonkhano wa anthu okhuzidwa mu pulogalamuyi, anthu a ku Kampaniyi azafotokozera onse oitanidwa m'mene malamulo a maiko, m'dziko, kapena m'dera angazatsatidwire mwa ntchuntchu.

- Mfundo ya Chiwiri: Kupereka mwayi kwa anthu a m'dera mofanana kusatengera kuti ndi wamwamuna kapena wamkazi ndi kupeleka mphamvu kwa amayi: Kugwiritsa ntchito zipangizo za makono ngati m'lowa-malo mwa zipangizo za chikale kuchepetsa kugwiritsa

ntchito makala/nkhuni zambiri zomwe zili ndi ubwino kwa amayi. Ubwinowu uzapelekedwa bwino bwino pa tsiku la msonkhano wa athu onse okhuzidwa mogwirizana ndi cholinga cha chisanu cha mfundo cha chitukuko chokhazikika.

- Mfundo ya Chitatu- Umoyo wa M'dera ndi Chitetezo: Palibe chiopsezo chili chonse choononga umoyo wa m'dera pamene zochitika za pulogalamu zayamba. Oyendetsa ntchito imeneyi azaonetsetsa kuti zochitika zake zonse zikulumikazana ndi anthu powafotokozera za ndondomeko zonse za chitetezo, komanso ndondomeko zotetezera ogwira ntchito kwa anthu amene alembedwa muzochitika za pulogalamu imeneyi.

- Mfundo ya Chinayi: Chikhalidwe cha anthu, Mbadwa za M'dera, Kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa: Cholinga cha pulogalamu ndi kukhazikitsa zipangizo zophikira za makono, kotero palibe chiopsezo chakuti itha kazaononga kapena kusokoneza chikhalidwe anthu. Otsogolera pulogalamu azaonetsetsa kuti zochitika zake zikutsatira zofunikira zonse. Anthu onse okhuzidwa azauzidwa mfundo zonse za chitetezo monga;
-Kuteteza malo a chikhalidwe cha anthu komanso osasokoneza mbiri yake
-Kupewa kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa kwa nzika za m'dera.
-Malamulo okhuza malo ndi ufulu wina uli wonse
-Ufulu wa mbadwa za m'dera.

- Mfundo ya Chisanu: Ziphuphu: Otsogolera Pulogalamu izaonetsetsa kuti zochitika zake sizikulimbikitsa ziphuphu komanso anthu akufotokozeredwa za kuipa kochita ziphuphu komanso kuuzidwa kuti BURN sizalekerera mtundu uli wonse wa ziphuphu pamene ntchito za pulogalamu zokhazikitsidwa.

- Mfundo ya Chisanu ndi Chimodzi: Zotsatira za Chuma: Pulogalamu izalemekeza ufulu wa anthu ogwira ntchito. Sizalekelera mchitidwe ogwiritsa anthu ntchito mwa ukapolo kapena kuphwanya malamulo a ntchito ovemelekezeka ndi maiko. Zochika zonse zizatsata mfundo ya chisanu ndi chimodzi yoyenera mu Gold Standard Safeguarding Principles.

**Chilengedwe ndi Ubale wa Zolengedwa Zonse**

Mfundo ya chisanu ndi ziwiri: Nyengo ndi mphamvu za Chilengedwe

- Kuika Utsi mlengalenga: Pulogalamu ichepetsa kuika utsi mlengalenga omwe umasokoneza nyengo kuchokera mmene ulili pano ndi kufika zaka khumi ziwiri zikubwerazi. Luso lomwe laikidwa lithandiza kupewa kuika utsi wambiri wa kaboni daiokisaidi mlengalenga.
- Mphamvu Zachilengedwe: Cholinga cha pulogalamu kukhazikitsa luso la makono logwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku zachilengedwe zosabwerezeka zochepa po phikira. Motero, kuchuluka kwa mitengo yodulidwa kuchokera nkhalango kuzachepa kusiyana ndi m'mene zili pano.

**Mfundo ya chisanu ndi zitatu: Madzi**

- Zotsatira za kuyenda kwa Madzi: Pulogalamu sizaonga madzi, kusokoneza m'mene madzi amayendera, komanso kupangitsa makomo kuti asowe madzi kapena kukokoloka kwa nthaka.
- Kukokoloka Kwa Nthaka: Pulogalamu ichepetsa kugwiritsa ntchito nkhuni kotero iteteza nkhalango. Pa chifukwa chimenechi, kukokoloka kwa nthaka kuzachepa ndipo madzi sazayenda mothamanga.
- Mfundo ya chisanu ndi zinayi: Chilengedwe, Ubale wa zolengedwa, ndi kagwiritsidwe ntchito ka malo.
- Kugwiritsa Ntchito Malo kapena Nthaka: Palibe mbewu iliyonse yomwe ingazalidwe ngati gawo limodzi la pulogalamu imeneyi.
- Chiopsezo ku Ngozi ya chilengedwe: Palibe zotsatira zili zonse zomwe pulogalamu ingathandizire kubweretsa ngozi ya chilengedwe.
- Kubweretsa Mbewu za Genetiki: Palibe kugwiritsa ntchito mbewu kapena zinthu zopangidwa mwa Genetiki zomwe zimaopseza chilengedwe.
- Kutulutsa zonyasa zoononga Chilengedwe: Malingana ndi zochitika za pulogalamu, kugwiritsa ntchito nkhuni/makala kuzachepa, kotero palibe kugwiritsa ntchito mafuta ambiri ochokera kuzotsalira zachilengedwe. Motero, palibe chiopsezo chotulutsa zonyasa zomwe zimaononga chilengedwe.
- Kutaya zinyalala ndi zina zoopsa: Panthawi yopanga mbaulazi, pulogalamu izagwira ntchito ndi makampani a m'dera ndipo izatsata malamulo oteteza kutaya zinyalala ndi zina

zoopsa ku chilengedwe. Pulogalamu izakhazikitsa ndandanda wabwino wa m'mene zinyalala azisamalira mu nthawi yonse imene ikugwira ntchito.

- Fetereza ndi Mankhwala Ophera Tizilombo: Palibe njira ina iliyonse yomwe Pulogalamu ingazagwiritse ntchito fetereza kapena mankhwala ophera tizilombo m'munda pa zochitika za ntchito zake.
- Kukolola Mitengo: Pulogalamu ichepetsa kufunikira kwa mitengo pophikira kotero iteteza nkhalango zanthu m'dziko muno.
- Chakudya: Pulogalamu ilibe chiopsezo pa chakudya kapena kusokoneza kulima kwa chakudya.
- Ulimi wa Ziweto: Pulogalamu sikukhuzana ulimi wa ziweto.
- Kusamala za chilengedwe zosiyana-siyana m'malo ake: Ntchito ina iliyonse ya pulogalamu izayenera kusonyeza kuti ikutsata ndi kuteteza za chilengedwe zonse m'malo ake molingana ndi malamulo a dziko komanso ndondomeko zomwe maiko onse oyenera kutsata.
- Zolengedwa zomwe zili pa Chiopsezo: Pulogalamu ilibe kuthekera koika chiopsezo kapena kusokoneza zolengedwa malo ake. Ntchito zake zizakhala makomo komaso mabungwe.
- Kubweretsa Mtundu wa chilendo wa mbeu: Palibe mtundu uliwonse wa mbewu kapena zomera zomwe zizayambitsidwe mu pulogalamu imeneyi.